Baibulo ya ana
Ikupasilani

Pasaka woyamba

Yolembedwa ndi: Edward Hughes
Yojambulidwa ndi: Janie Forest
Alastair Paterson
Yotengedwa ndi: Lyn Doerksen
Yotathauzidwa ndi: Phiri Williams
Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

BFC
PO Box 3
Winnipeg, MB R3C 2G1
Canada

©2020 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Mkazi anaima pamwamba
papiri la phokoso,
ndi maso odandawula
amayangana
zinthu zowopsya
zimachitika.
Mwana wake
amamwalira.
Mayi yu anali
Maria, ndipo
anaima pafupi
ndi malo pomwe
Yesu anali
kukhomedwa
pamtanda.





Kodi zonsezi zinachitika bwanji? Kuti Yesu athetse moyo wake wokongola munjira yoyipa ngati imeneyi? Kodi Mulungu analola bwanji kuti mwana wake akhomedwe pamtanda ndikufera pamenepo? Kodi Yesu analakwitsa kukhala yemwe analili? Kodi Mulungu analephera?

3

Ayi! Mulungu sanalephele. Yesu sanalakhwisa konse. Yesu nthawi zonse amadziwa kuti anthu oipa adzamupha. Ngakhale pomwe iye anali mwana, munthu wina wochedwa Simioni anamuuza Maria za nkhani yosakondweretsa inali patsogolo pawo.

4

Patatha masiku ochepa Yesu asanaphedwe, Mzimai anabwera ndimafuta nadzoza Yesu mapazi ake. "Akuwononga ndalama" wophunzila ake anadandaula. "Wapanga nchito yabwino" Yesu anayankha. "Wapanga izi zakuyikidwa kwanga m'manda." Mawu otani achilendowa!

5

Patatha izi, Yudasi, mmodzi wawophunzira a Yesu khumi ndi awiri, anavomereza kumpereka Yesu kwa akulu ansembe ndi ndalama zitatu zasiliva.

6

Paphwando la chi Yuda, Yesu anali nawo kudya komalizira ophunzira ake. Anawauza zabwino za Mulungu malonjezo kwa iwo omukonda iye. Ndipo anapereka mkhate ndi chikho kuti agawane. Uku kunali kuwakumbutsa za thupi ndi mwazi woperekedwa ku chikhululukilo cha machimo.

7

Kenaka Yesu anawawuza anzake kuti azaperekedwa, ndikuti iwo azamthawa. "Ine sindiza thawa," Petulo ananena. "Tambala asanalile, udzanikana ine katatu," Yesu ananena.



8

Kenaka usiku, Yesu anapita kukapemphera kumunda wa Getsemani. Wophunzira amene anali naye anagona tulo. "Atate wanga," Yesu anapemphera, "...mulole chikho chamasautso chindipitilire. Koma, sikufuna kwanga, chifuniro chanu chichitike."

9

Mwazizizi chiguru cha anthu chinabwera ku munda, chotsogoleredwa ndi Yudasi. Yesu sanadziletse ayi, koma Petulo anadula khutu la munthu wina. Mwakachete chete, Yesu anabwedzeretsa khutu la munthu uja. Yesu anadziwa kuti kuperekedwa kwake kunali chifuniro cha Mulungu.



10

Guru linamtenga Yesu ku nyumba ya mfumu yayikulu. Kumeneko, atsogoleri achi Yuda anati Yesu aphedwe. Pambaripo, Petulo anayima akuwota moto ndi kumayanganira. Katatu anthu anamyangana Petulo nati, "iwe unali ndi Yesu!" Katatu konse Petulo anamkana, momwe Yesu anamuuzira. Petulo analumbira ndi kutemberela.

11

KOKO-RI-KOKOOO

Pompo, Tambala analira. Zinakhala ngati Mulungu wayankhula kwa Petulo. Ankumbukira mawu a Yesu, Petulo anabuula kowawa.

12



Yudasi anadandaula, nayenso. Anadziwa kuti Yesu analibe chimo lililonse ngakhale mulandu uliwonse. Yudasi anabwedzera ndalama masiliva atatu aja, koma ansembe anakana kutenga ndalamazo. Yudasi anaponya ndalamazo pansi, naturuka-ndikukazimangirira yekha.

13

Ansembe anamtenga Yesu kupita naye kwa Pilato, kuboma la chi Roma. Pilato anati, "ine sindinapeze kulakhwa kwa munthuyu." Koma guru linapitiliza kupfuula, "mpachikeni! Mpachikeni!"

14

Pomalizira Pilato analola, nalamula kuti aphedwe. Asilikali anammenya Yesu, namlavulira malovu komanso, namkwapula iye. Anasoka chipewa chaminga nachikanikiza pamutu pake. Kenaka namkhomera pamtanda kuti afe.



15

Yesu amadziwa kuti ndi njira yomwe adzafere. Anadziwanso kuti imfa yake idzabweretsa chikhululukiro kwa ochimwa womkhululupira iye. Mbava ziwiri zinakhomedwa mbali mwa mtanda wa Yesu. Mmodzi anakhulupirira Yesu – na pita ku paradiso. Winayo sanathe.



16

Patapita mawola yamasautso,Yesu anati, "Kwatha," namwalira. Nchito yake inakwaniritsika. Anzake anamuyika mmanda.



17

Ndipo asilikali achi Roma anatsekapo pamandapo ndikumalondela mandawo. Ndipo kunalibe angalowe – kapena kuturuka.

18

Ngati kunali kumaliza kwa nkhaniyi, zikanakhala za chisoni. Mulungu anapanga chodabwitsa. Yesu sadakhalilirebe wakufa!

19

M'mamawa tsiku loyamba la sabata, ophunzira a Yesu anapeza mwala utachotsedwa pamanda. Pomwe anapenya mkatimo, Yesu munalibemo.

20

Mzimayi wina anakhalila, amalira pamandapo. Yesu anawonekera kwa iye! Anathamanga mokondwera kukawuza wophunzira ena. "YESU ALI NDI MOYO! YESU WAUKA KWA AKUFA!"



21

Kenaka Yesu anawonekera kwa ophunzira ake, ndi kuwawonetsa mabala ake mmanja. Zinali zoona. YESU ALINDIMOYONSO! Anamkhululukila Petulo pamene anamkana iye, nawuza ophunzira ake kuti auze anthu onse za iye. Kenako anabwelera kumwamba komwe anachokela nthawi yoyamba ija ya Khrismasi.

22

Pasaka woyamba

Nthano yochokera mu mau a Mulungu,
Baibulo,

opezeka mu

Mateyu 26-28, Luka 22-24, Yohane 13-21

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

23

Mapeto

54 60

24

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16

25